Pewani Nsanje

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwa, yerekezani kuti inuyo mukuona pamene nkhaniyo ikuchitika. Yesani kuona m'maganizo mwanu zimene zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a m'nkhaniyi akumvera mumtima mwawo.
Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi: Miriamu, Aroni ndi Mose
Chidule cha nkhaniyi: Miriamu ndi Aroni anachitira nsanje m'bale wawo Mose n'kuyamba kumunena.

1 GANIZIRANI ZIMENE ZINACHITIKA.—WERENGANI NUMERI 12:1-15.

Kodi mukuganiza kuti anthu atatuwa ankaoneka bwanji, ndipo anali ndi makhalidwe otani?

Miriamu: _____

Aroni: _____

Mose: _____

Kodi mukuganiza kuti mawu amene Miriamu ndi Aroni ananena, omwe ali pavesi 2, anamveka bwanji?

_____

Yesani kuona mmene 'mtambo woima njo ngati chipilala' unkaonekera ndiponso ganizirani mmene mawu a Yehova ankamvekera pamene anadzudzula Miriamu ndi Aroni. Fotokozani zimene mukuona ndiponso kumva m'maganizo mwanu. **(Werenganinso Numeri 12:5-9.)**

_____

Malinga ndi vesi 11 mpaka 13, kodi mukuganiza kuti Aroni ndi Mose ankamva bwanji pamene anachonderera Yehova kuti achiritse Miriamu?

_____

2 FUFUZANI MOZAMA.

Kodi anali wamng'ono ndani pakati pa Miriamu, Aroni ndi Mose? Kodi mukuganiza kuti zimenezi zinakhudza bwanji mmene Miriamu ndi Aroni analankhulira ndi m'bale wawo? Fotokozani. (Werengani Ekisodo 2:1-4, 10; 7:7.)

_____

N'chifukwa chiyani Miriamu ndi Aroni anafunsa kuti: "Kodi [Yehova] sanalankhulenso kudzera kwa ife?" (Zokuthandizani: Werengani Ekisodo 15:20, 21; 28:1-3.)

_____

N'chifukwa chiyani Yehova anakwiya kwambiri ndi Miriamu ndi Aroni?
(Werengani Numeri 12:7, 8.)

_____

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

N'chiyani chakusangalatsani mukaganizira zimene Mose anachita atatsutsidwa?

_____

_____

_____

3 GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA.

Lembani zimene mwaphunzira zokhudza . . .

Kuopsa kwa nsanje.

_____

_____

Zimene mungachite ena akakunenani popanda chifukwa.

_____

_____

4 DZIFUNSENI KUTI:

N'chiyani chingachititse kuti ndiyambe kukhala ndi mtima wansanje?

_____

_____

Kodi ndingatani kuti ndizichita zinthu modekha ndiponso mwachikondi ndikamatsutsidwa?

_____

_____

M'nkhaniyi, kodi ndi mfundo iti imene yandikhudza mtima kwambiri, ndipo n'chifukwa chiyani?

_____

_____

Mungachite izi: Werengani nkhaniyi mokweza limodzi ndi anzanu kapena anthu am'banja lanu. Munthu wina awerenge mavesi ofotokoza nkhaniyi. Anthu ena awerenge mawu a Miriamu, Aroni, Mose ndiponso Yehova.

JW.ORG™

Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania